

Kulalikira (Preaching)

Kulalikira ndi kulengeza Mau a Mulungu kwa anthu omwe aitanidwa ndi Mulungu. Ndi njira yokhayo imene Mulungu amalankhulira Mau ake kwa anthu. Kulalikira ndi kofunika kwambiri kuti mpingo uyende bwino. Mpingo umakhala ofooka ndi osalongsoka ngati palibe kulalikira koono kwa Baibulo.

1. Kulalikira m'chiyani?

Chipangano Chatsopano chimatchura mawu oti “kulalikira” koposa makumi asanu ndi limodzi. Alipo mau okwana anayi a Chigiriki m'Chipangano Chatsopano otanthauza kulalikira.

- A. Mau oti **Kerusso** amatanthauza mthenga kapena kulengeza uthenga wa mfumu. Zomwe zikutanthauza kuti olengezayo salengeza uthenga wake, iye amalengeza pansu pa ulamuliro wa amene antumiza. Mlaliki ayenera kuitanidwa ndi Mulungu ndipo ayenera kulamulidwa ndi Mulungu.
 - B. Mau oti **Evangelizo** amatanthauza kulalikira kapena kupereka uthenga wabwino. M'ngelo Luka 2:10 akulalikira pamene akupereka uthenga wabwino. Zikutanthauza uthenga wabwino.
 - i. Mawu oti **Kerusso** ndi **Evangelizo** akugwiritsidwa ntchito m'ndime imodzi (Luka 4:18-19). Yesu anagwiritsa ntchito mau oti **Kerusso** m'gawo loyamba la vesi 18 ndipo **Evangelizo** m'gawo lomaliza la vesi 19. Luka 4:18-19 “Mzimu wa Mulungu uli pa Ine.” Chifukwa chake anandidzodza Ine “kulalikira [**Kerusso**]” am'nsinga mamasulidwe, ndi akhungu kuti apenyenso, kutulutsa ufuru ophwanyika. (Luka 4:19) “kulalikira (**Kerusso**) za chaka cha Ambuye.”
 - C. **Martureo** kuchitira umboni. Olalikira amapereka umboni wa m'Baibulo.
 - D. **Didasko** kutanthauza kuphunzitsa mau a uthenga pa zomwe zikutanthauza kwa omvera. Tingatinso mlaliki amafotokoza zomwe Baibulo likunena kuti omvera aphunzire kanthu kena m'moyo wake, ndipo asinthe moyo wao mogwirizana ndi Baibulo.
2. Pamene mlaliki akulalikira amagwiritsa ena a mau awa mu uthenga wake. Mwachitsanzo (Machitidwe 15:35), timawerenga kuti Paulo ndi Barnaba analalikira; kuphunzitsa ndi kulalikira mau a Mulungu. Ndime zina za Baibulo zomwe mlaliki akugwiritsa ntchito mau oposa awiri ndi (Machitidwe 28:31) Paulo anagwiritsa ntchito mau oti kulalikira komanso kuphunzitsa (**Kerusso** ndi **didasko**).

A. Kulalikira ndi Kuphunzitsa

II. Kodi kulalikira kwabwino ndi kotani?

1. Kasanthura mau zikutanthauza kepereka tanthauzo lenileni la mau ndi ziganizo. Mlaliki afotokoze molondora zomwe Baibulo likunena. Olemba Baibulo anali ndi tanthauzo limodzi ndipo olalikira apereke tanthauzolo. Palibe chinthu chopambana kwambiri pa ulaliki kuposa kupereka molondora zomwe Baibulo likunena.

- A. Pemphero ndi lofunika kwambiri pa ulaliki. Nthawi yomwe mumapemphera ndi yofunika pokonzekera ulaliki.
- B. Ndongomeko zopezera tanthauzo lenileni la ndime ya Baibulo. Nthawi yopambana kwambiri pa ulaliki sinthawi yolalikira, koma nthawi yomwe mumakonzekera ulaliki monga kupemphera.
 - i. Mulungu amafuna mlaliki kupereka ulemu ku Baibulo chifukwa ndi Mau a Mulungu. Amayembekeza mlaliki kukumbukira kuti Baibulo liri ndi tanthauzo lapadera ndipo tanthauzolo ndi la Mulungu osati tanthauzo limene mlaliki akufuna.
 - ii. Tiyenera kuwerenga mau onse ndi kuvomereza matanthauzo ake.
 - iii. Tiyenera kudziwa mtundu wa ndime yomwe ife tikufuna kulalikira monga mbiri kapena ndakatulo etc.
 - iv. Tiyenera kudziwa chomwe chinkachitika panthawiyo, mwachitsanzo (1Akolinto 2:6-11). Anthu ambiri amalankhula za kumwamba pa ndime imeneyi, koma uku nkulakwitsa chifukwa apa ndime sikufokoza za kumwamba. Ndimeyi ikufotokoza kuti anthu a Mulungu akhoza kuona ndi kuyamika zinthu za uzimu zomwe ziri zobisika kwa anthu osapulumsidwa.
 - v. Tiyenera kudziwa za mbiri (chomwe chinkachitika pa nthawiyo). Chitsanzo ndi chomwe chikupezeka pa Machitidwe 19:1-2), pomwe Paulo anafunsa atsogoleri a chipembedzo ngati analandira Mzimu Woyera ndipo anati, “ayi” lomwe linali yankho loyenera pa nthawi ya Abraham. Komabe pa Machitidwe 19 Pentecoste atapita mpingo unapatsidwa Mzimu Woyera; kuyankha kuti “ayi” kumatanthauza kuti iwo sanali akhristu pakuti Paulo analankhura ndi anthu osatembenuka mtima zomwe zinawatsogolera iwo kukutembenuka mtima.
 - vi. Kodi Mau a ndime zina za Baibulo akutiuzwa chiyani? Tiyenera kugwiritsa ntchito Mau a Mulungu kumasuliranso Mau a Mulungu. Mwachitsanzo, simungalalikire za Mekizedeki pogwiritsa ntchito Genesis 14:18-24 yekha. Muyenere kulalikiranso Aheberi 5:5-10 ndi 7:1-28.
 - vii. Kodi ndime imeneyi ikunena chiyani za Khristu? Baibulo lonse limatilozerwa kwa Khristu ndipo ulaliki ulionse uyenera kuloza kwa Khristu. Nthawi zina zimakhala zovuta kupeza izi, koma muyenera kuyang’anitsitsa; mwachitsanzo buku la Mlaliki limatidabwitsa ndikutipangitsa ife kukhala ndi njala ya Mau a Mulungu.
 - viii. Kodi ndingasanthure bwanji Mau a Mulungu zomwe zikutanthauza kuti kodi tingagwire bwanji ntchito yofotokozera bwino Mau a Mulungu? Nanga tingagwire bwanji ntchito yofotokozera zomwe Baibulo likunena? Tingachite izi powerenga Baibulo ndi kupemphera kuti timvetsetse bwino.

2. Ziphunzitsa ndi zofunikira

- A. Ulaliki uyenera kukhala ndi ziphunzitsa za Baibulo. Apa zikutanthauza kuti tiyenera kuphunzitsa za chilengedwe, chiombolo, chiweruzo, zakumwamba, Gehena, ndi zina.
- B. Maulaliki anthu ayenera kuthandizira kumvetsetsa ndondomeko za choonadi cha ziphunzitsa za Baibulo (Aroma 6:17).
- C. Kodi chimachitika m’chiyani ngati ziphunzitsa za Baibulo sizikuphunzitsidwa?
 - i. Mulungu salambiridwa kapena kukondedwa monga Iye ayenera chifukwa anthu satha kumumvetsetsa Iye. Sadziwa za Mulungu wodabwitsa,

wamphamvu, ndi wachikondi yemwe iwo ali naye. Anthu amalephera kuyamika Mulungu.

- ii. Anthu sadziwa ubale wodabwitsa umene uli pakati pa anthu ndi Mulungu.
 - iii. Okhulupilira sadziwa za maufulu awo ngati akhristu.
 - a. Anthu sadziwa za madalitso omwe ali nawo chifukwa chakulungamistidwa kwao zomwe zimatanthauza kuti amakhululukidwa machimo awo ndipo amayembekezera kumwamba.
 - b. Anthu sadziwa kuti ndi ana a Mulungu ndipo ali ndi maufulu monga ana a Mulungu.
 - c. Anthu sakondwera ndi phindu lakukhala monga ana a Mulungu. Kukhala pakati pa anthu omwe ndi akhristu mkwabwino koposa kukhala pakati pa anthu omwe si okhulupilira.
 - iv. Akhristu sakhala ndi chitsimikizo chachikhalidwe chao. Tikuyenera kumvera Mulungu ndipo kuti timvere Iye timayenera kum'dziwa Iye. Ndi udindo wa mlaliki kuphunzitsa malamulo a Mulungu.
 - v. Kupereka umboni pa zomwe Mulungu wakuchitirani kumakhala kovuta. Okhulupilira sadziwa choti alankhule kuti anthu ena athe kutembenukira kwa Mulungu. Alaliki ayenera kuphunzitsa omvera zakulalikira.
 - vi. Anthu sadziwa m'mene angakhalire bwino.
 - vii. Anthu sadziwa m'mene angapemphelere bwino.
3. Kulalikira kuyenera kukhala kwandondomeko ndi komveka bwino. Ulaliki uyenera kugwirizana ndi uthenga weniweni wa ndime yosankhidwa. Ulaliki uyenera kukhala ndi ndongosolo lomwe liyenera kutsatiridwa bwino. Magawo alionse ayenera kutsatidwa pa ulaliki. Mbali zomwe ziri zosafunika kweni kweni ziyenera kusamalidwa polalikira. Mwachidule ulaliki uyenera kukhala wadongosolo.
- A. Chiyambi. Awa ndi mau oyambilira omwe anthu amauzidwa ndi zolinga za ulaliki kuti anthu athe kutsatira bwino. Nthawi zina zimachitika powauza nkhani yogwirizana ndi ulalikiwo.
- i. Chiyambi sichiyenera kukhala chachitali chifukwa sigawo la ulaliki koma ndi gawo chabe lomwe limayamba chigawo cha ulaliki.
- B. Kufotokozero. Chiyambi chikatha ndi nthawi yoti gawo lalikuru la ulaliki lomwe likufotokoza za choonadi lilalikidwe.
- i. Muyenera kukhala ndi chikonzero. Malingaliro anu ayenera kuperekedwa m'dongosolo loti anthu athe kuona kuti mukuchokera kuchiyambi mpaka pa mathero. Chikonzero chikhale chosavuta ndi cholinga choti aliyense amvetsetse. Chomwe muyenera kudziwa m'chakuti cholinga cha ulaliki ndi kuti aliyense amve uthenga umene ukulalikidwa.
 - ii. Kufunikira kwa zigawo. Muyenera kukhala ndi mfundo zitatu kapena zinayi; ngati nkofunikira lalikirani mutu wanu kwa masabata angapo m'malo molalikira ulaliki wautali pasabata imodzi.
 - iii. Kufanana. Onetsetsani kuti gawo lirilonse mwalipatsa nthawi yofanana. Ndipo ngati mukulalikira kwa maminitsi makumi anayi (40 min), onetsetsani kuti simunalalikire maminitsi makumi atatu pa mfundo imodzi.

iv. Kukakamiza. Mfundo ziziperekedwa bwino. Mateyu 6:1-18 Yesu akuphunzitsa ntchito za chifundo, pemphero ndi kusala. Poyamba akuwauza anthu chomwe sayenera kuchita kenako chomwe ayenera kuchita. Yambani ndi zinthu zomwe ziri zoipa kenako zabwino.

v. Chikoka (chidwi). Tikhoza kupanga ulaliki kukhala wochititsa chidwi polankhula mau omveka bwino. Yesetsani kuti ulaliki wanu ndi wachikoka.

C. Mathero

i. Tanthauzo la mathero. Mathero anu ayenera kupereka chidule cha ulaliki wanu ndi kumangiriza zonse pamodzi.

ii. Kufunikira kwa mathero. Mathero abwino ayenera kukhala a chidule ndi achilimbikitso. Mathero abwino amachita chidule cha ulaliki ndipo nthawi zina chilimbikitso chachifupi kapena chikumbutso cha magawo akuru aulaliki. Mathero abwino ndi chinthu chokhacho chimene munthu amakumbukira mu ulaliki wanu.

iii. Malangizo. Lembani zomwe mukaganiza kuti anthu asaziiwale. Mathero anu amakhala mu mtima mwanu musanamalize ulaliki wanu. Mathero anu amakhala a omvera komanso nokha.

4. Zitsanzo zopezeka. Tsopano aliyense wadziwa kuti kulalikira ndi ntchito yaikuru.

A. Chitsanzo ndi mau a chithuzi chomwe chimathandiza kumvetsetsa bwino. Pali mwambi oti Chitsanzo chimaposa mau oposa chikwi. Chitsanzo cha mau ndi pamene mau akuperekedwa m'njira yomwe imapanga womvera kukhala ndi chithunzi ndi kumvetsetsa zomwe olankhula akufotokoza.

i. Kawirikawiri timakhala ndi zithunzi m'mitima yathu kuchokera kumawailesi pamene nkhani ikunenedwa monga uthenga umenene umagwiritsidwa ntchito kuthetsa ziwawa.

B. Zithunzi za mau zimathandiza kufotokozerera choonadi mwa chitsanzo Mateyu 13. Onani mavesi 23, 31, 33, 44, 45 47. Paulo ntumwi m'buku la Aroma 6 ndi 7 pamene akunena kuti akhristu sayenera kukhala mu uchimo chifukwa si ifenso akapolo a tchimo. Akugwiritsa chitsanzo cha msika wa ukapolo kumene kukhoza kudza mwini wa kapoloyo; tiyenera kukhala mosonyeza kuti Khristu ndi Mbuye wathu.

C. Zitsanzo za mau zimathandiza kupanga ulaliki wathu kukhala wochititsa chidwi kotero kuti anthu amamvetsera mwachidwi. Anthu akamva mlaliki kwa kanthawi amasiya kumvetsera, chidwi chao chimatha ndipo maganizo awo amatembunukira kumaganizo ena. Pamene kukugwiritsa ntchito chitsanzo mkati mwa ulaliki wanu mumapangitsa anthu kukhalabe ndi chidwi

D. Zitsanzo zimathandiza munthu kukumbukira mfundo zikuruzikuru za ndimeyo. Ngati mukukhala ndi chitsanzo, zimathandiza anthu kukumbukira kuposa mau okha. Chitsanzo ndi fanizo lomwe likupezeka m'buku la Luka 15 la mwana olowelerera yemwe anadziwa kuti ayenera kubwerera kwa Atate wake. Vesi 23 likufotokoza za chisangalalo cha Atate kuti mwana anali kubwelera kwa Atate ndipo anakonza phwando. Apa zikuthandiza kuti

anthu akhale ndi chithunzi m'mitu mwao. Mukhoza kupanga chimodzimidzi pofotokozera za phwando la ukwati lomwe munakhala nalo. Zitsanzo za maukwati amenewa zikhoza kuthandiza anthu kukumbukira mfundo; Yesu amakondwera pamene m'modzi wa ana ake abwelera kwa Iye.

5. Phunziro la ulaliki. Ulaliki wanu uyenera kupangidwa poyang'anira anthu anu. Uyenera kuyang'anira pa zosowa za uzimu za akhristu; ndipo uyenera kulalikidwa malingana ndi m'mene anthuwo aliri kuti athe kugwiritsa ntchito zomwe aphunzirazo m'moyo wao watsiku ndi tsiku. Ulaliki wanu usamakhala ovuta kumvetsa.
 - A. Kodi tanthauzo la phunziro la ulaliki m'chiyani? Phunziro la ulaliki ndi gawo la ulaliki lomwe limasonyeza omvera m'mene angagwiritsire ntchito zomwe Baibulo likuphunzitsa m'moyo wawo; phunziroli limayang'ana pa omvera ulaliki.
 - B. Phunziro ndi lofunikira kwambiri ndipo ngati palibe ulaliki onse umakhala opanda pake. (Ulaliki opanda phunziro ndi kufotokoza mfundo zomwe ziribe phunziro lirilonse) Kumbukirani kuti cholinga chanu ndi kuphunzitsa. Alaliki ena amafuna kudzionetsa kuti iwo ndi ophunzira kwambiri; ndipo sasamala ngati omvera aphunzira zomwe zalalikidwazo. Phunziro ndi pokhapokha omvera aphunzira kanthu kena pa ulaliki wathu.
 - i. Chitsanzo cha phunziro la cholinga ndi kufotokozera zimene Baibulo likufotokoza m'ndime monga Genesis 12:1-9. Mlaliki afotokoze chomwe chinachitika pamene Mulungu analamulira Abram ku choka kwao pakupanga pangano ndi iye. Akhoza kufotokozera kuti nkhani imeneyi ikukhudza chikhulupiliro ndi kumvera; phunziro lokhoza kuphunzitsa omvera kudalira ndi kumvera Mulungu.
 - C. Nanga timapanga bwanji phunziro la cholinga?
 - i. Lalikirani mwachindunji. Onetsetsani kuti phunziro la ulaliki wanu likuperekedwa kwa omvera kuti amvetsetse chomwe chalalikidwa. Chitsanzo chikupezeka m'buku la Mateyu 19:12 pamene Yesu akumuuzza munthu mwini chuma choti achite. Yesu sanabise chomwe munthuyo anayenera kuchita.
 - ii. Adandaulireni. Musangonena kokha zomwe ayenera kuchita, komanso auzeni momwe angachitire nanga m'chifukwa chiyani ayenera kuchita zomwe mukufuna kuti iwo achitezo. Pamene mukupereka phunziro, powapempha anthu kulapa ndi kukhulupilira mwa Yesu pa chipulumutso chao, awuzeni anthu momveka bwino. Panthawi ya phunziro musalankhule za Gehena, m'malo mwake awuzeni anthu kudabwitsa kokhala ndi Yesu.
 - D. Mulingo womaliza wa kulalikira mpamene mukuona kusinthika kwa anthu omwe mukuwalikira.
6. Kupereka uthenga. Kupereka uthenga nkofunikira kwambiri, komatu sumakhala uthenga mpaka utalalikidwa; ndipo kupereka uthenga nkofunikira kwambiri kufanana ndi kukonzekera.

- A. Mzimu wanu ndi ofunikira kwambiri pamene mukulalikira.
- i. Mlaliki ayenera kukhala munthu olimba mtima. Ayenera kulalikira mwamphamvu ndi mosaopa uthenga wa Baibulo ndipo sayenera kudandaura ngati uthenga sunakondweretse omvera. Ayenera kukondweretsa Mulungu osati anthu. Musalikire kuti akondwere koma kuti anthu adziwe choonadi.
 - ii. Mlaliki akhale wodzichepetsa ndipo adziwe kuti iyenso ndi ochimwa ndipo dziwani kuti timakwaniritsa zinthu zonse m'mphamvu ya Mulungu.
 - iii. Tilalikire zooni. Uthenga wanu ukhale oona; ndipo mudzikhulupilira.
 - iv. Mlaliki azidziwa chomwe akulalikira.
 - v. Mlaliki azilimba mtima polalikira ngakhale uthengawo utakhala osasangalatsa anthu.
 - vi. Mlaliki azisonyeza kukhudzidwa ndi zimene akulalikira.
- B. Chiyankhulo. Tiyenera kusamalira ndi chiyankhulo chathu.
- i. Chiyankhulo chathu chidzikhala chomveka ndi wina aliyense.
 - a. Onetsani mfundo zanu m'ziganizo zomwe mukulankhula.
 - b. Ziganizo zanu zikhale zazifupi.
 - c. Gwiritsani ntchito mau omwe angamveke ndi onse.
 - d. Fotokozerani mau amene mukuganiza kuti omvera sanakumvetsetseni bwino.
 - i. Malamulo a chiyankhulo. Gwiritsani ntchito ziganizo motsatira malamulo achiyankhulo.
 - ii. Chilimbikitso. Sankhani mau omwe akhoza kukuthandizani kufotokozerani bwino zomwe mukulalikira.
- C. Liwu la mau anu. Gwiritsani ntchito mau anu enieni. Mukhoza kumasintha mau anu pokweza, kutsitsa, kufulumiza pamene mukulalikira cholinga chanu ndi kupanga uthenga wanu kukhala wochititsa chidwi. Nthawi zambiri kumapumira polankhula zimathandiza omvera kutsatira bwino ulaliki wanu. Musamangokuwa nthawi zonse.
- D. Lankhulaninso mosagwiritsa ntchito pakamwa. Tiyenera kudziwa kuti nthawi zina timatha kutumiza uthenga mosagwiritsa ntchito pakamwa. Timachita izi m'mene takhalira, tayimira, m'mene tikuyang'anira ndi m'mene tikugwiritsira ntchito manja athu.
- i. Kayang'anidwe. Muiyenera kumayang'ana anthu. Musamayang'ane kunja kapena m'mwamba pamene mukulalikira. Mudziwayang'ana anthu omwe mukuwalalikira kuti adziwe kuti mukulankhula ndi iwo.
- E. Maonekedwe anu. Muiyenera kuvala bwino mosonyeza ulemu kwa amene mukuwalalikira komanso Mulungu. Musavale zovala zoseketsa kapena zosalongosoka zimapangitsa anthu omvera kuleka kumvera nkumayang'ana zomwe inu mwavalazo.
- F. Nthawi. Musamalalikire chinthawi chachitali anthu amasiya kumvetsera. Lamulo labwino ndi kupereka uthenga kenaka nkuchokapo. Yambani ulaliki wanu nthawi yabwino.

Musadikilire anthu ochedwa. Anthu amanva uthenga nthawi yochepa yokha. Mauthenga ambiri amasokonezeka chifukwa olalikira sanachoke pamene iwo amayenera kutero.

7. Kulankhula mwa chikoka ndi kulankhula mwakaso ndi mochtitsa chidwi.
- A. Ngati cholinga chanu ndi kuona mau a Mulungu akusintha anthu muyenera kupempha Mzimu Woyera kuti ukwaniritse izi. Ndi mphamvu ya Mzimu Woyera imene imasintha anthu (1 Atesolonika 1:5).
- B. Kufunika kwa moyo wanu wa uzimu. Muyenera kukhulupilira kuti uthenga wanu ndi wofunikira kwambiri ndipo uyenera kuperekedwa (2 Akolinto 4:13). Anthu akumwalira opanda Khristu m'moyo mwao ndipo akuyenera kumva za Iye asanamwalire. Muyenera kukhulupilira kwambiri kufunika kwa uthenga wanu kuti simuyenera kudikilira mpaka mutapereka uthengawo.
- C. Monga ndafotokoza kale, uthenga wanu uyenera kukhala opambana kwambiri kwa inu, kotero izi zikupangitseni kuperekanso kwa anzanu.

III. Uthenga omwe tikukonzekera kulalikira

1. Musadikire mpaka nthawi yomaliza. Ngati mumalalikira sabata iriyonse yambani kukonzekera mukangotsiriza kulalikira uthenga wanu. Apa ndikutanthauza yambani kusonkhanitsa maganizo anu pa zomwe mukufuna kudzalalikira sabata ya mawa.
 - A. Ndondomeko zomwe muyenera kuzitsata:
 - i. Muyenera kukhala ndi nthawi yosinkhasinkha, kupemphera ndi kudikilira Mulungu pa zomwe mukufuna kudzalalikira. Pemphero ndi chinthu chopambana kwambiri kuti muthe kulalikira uthenga wabwino. Zimapezeka nthawi zina kuti pamene tangoyamba kuwerenga mau zonse zomwe tinakonzekera zasokonezeka (zaiwalika). Mwina mfundo zimene munasonkhanitsa zimabalalika. Yambani mwa ima, pempherani ndipo mveterani. Nthawi zina tikhoza kusintha ndime yomwe tinakonzekera. Kenaka tidzaona kuti uthenga onse walalikidwa bwino.
 - ii. Sinkhasinkhani za ndime yomwe mwaisankha. Werengani Baibulo lanu kwambiri.
 - iii. Yambani kulemba. Panthawiyi musafulumire kusonkhanitsa mabuku anu, lembani kaye maganizo anu.
 - iv. Sonkhanitsani mabuku anu moyang'anira mfundo zomwe mwazilemba.
 - v. Chitani kafukufuku wa zomwe mwachita. Onetsani kuti:
 - v.a. Mukufotokozani tanthauzo lenileni lomwe olemba anali kulipereka; onetsani kuti uthenga wanu ukulozera kwa Khristu.
 - v.b. Uthenga wanu ukupereka chiphunzitso chomwe chikuyenera kulalikidwa pa ndimeyi.
 - v.c. Uthenga wanu walembedwa mwatsatanetsane kuti aliyense athe kuutsata bwino.
 - v.d. Muli ndi chitsanzo chomwe mukufuna kuchipereka kuti anthu achite nacho chidwi.

v.e. Muli ndi phunziro lomwe mwaliyika mu uthenga wanu lomwe likhoza kusintha moyo wa omvera akagwiritsa ntchito zomwe amvazo.

- vi. Lembani ulaliki wanu komaliza kukonzekera kulalikira.
- vii. Pemphererani ulaliki wanu kuti Mulungu akusintheni komanso akathe kusintha omvera. Pemphani kuti Mulungu adalitse uthenga wanu. Pemphani kuti uthenga usinthe inu komanso omvera. Pemphani Mulungu kuti alankhule nanu ndipo thokozani Mulungu chifukwa cha uthenga wanu wabwino.
- viii. Lalikirani ulaliki wanu mosamala ndi mochititsa chidwi.
- ix. Onetsetsani chomwe chachitika utatha ulaliki wanu, nthawi zina mumakhala nokha. Fufuzani izi pa ulaliki ulionse.

VI. Mathero

1. Yambani kukonzekera ulaliki wanu mwansanga. Ine ndimayamba kukonzekera kwa mwezi wathunthu.
2. Timayenera kukhala ndi nthawi yokwanira yokonzekera. Abusa omwe akhala akulalikira zaka zambiri amakhala ndi nthawi yochepa yokonzekera kulekana ndi amene angoyamba kumene. Konzekerani kwa tsiku lathunthu. Musafulumire ndi cholinga chongofuna kumaliza.
3. Kumbukirani kuti awa ndi mau a Mulungu omwe mukufuna kugawana ndi omvera.